

# Phunzirani kwa Ena

Sankhani zimene mukuona kuti n'zogwirizana ndi ana anu. Mukambirane zinthuzo monga banja.

## ZIMENE MUNGASINDIKIZE




### ZOTI BANJA LIWERENGERE PAMODZI

**NKHANI YA M'BAIBULO:** Werengani nkhani ya Zithunzi Zofotokoza Nkhani ya M'Baibulo, yamutu wakuti “Loti ndi Banja Lake.” Kenako kambiranani mafunso amene ali kumapeto kwa nkhaniyo.



### MAFUNSO

**KULALIKIRA PADZIKO LONSE:** Werengani Aroma 10:13-15. Gwiritsirani ntchito zithunzi, mapu ndi “Mfundo Zachidule” zimene zimapezeka patsamba loyamba la pa [jw.org](http://jw.org) kuti mufufuze malo komanso kuphunzitsa ana anu zokhudza mayiko ena.



### VIDIYO

**ZIMENE ACHINYAMATA ANZANU AMANENA:** Za ana a zaka za pakati pa 10 ndi 12. Onerani vidiyo yachingelezi yamutu wakuti “What Your Peers Say—Sexual Harassment.” Kenako kambiranani mafunso atatu amene ali pa vidiyoyo.



### ZOTI MUCHITE POPHUNZIRA

**MAFUNSO A M'BAIBULO:** Pitani pagawo la [jw.org](http://jw.org) lakuti “Kuyankha Mafunso a M'Baibulo.” Mukafika pamutu wakuti “Pemphero,” uzani ana anu kuti asankhe funso limene akuona kuti akhoza kufunsidwa ndi anthu omwe amakhulupirira zosiyana ndi iwowo. Mukawerenga yankho la funsola, athandizeni anawo kuti asankhe lemba limene angawerenge poyankha funsola. Kenako auzeni kuti alembe mawu amene anthuwo akulankhula.